


GREAT PASSAGES OF THE BIBLE (CHINYANJA)
PUBLISHED BY THE BAPTIST PUBLISHING HOUSE
BOX 31995, LUSAKA, ZAMBIA



**NDIME ZA ZIKURU-ZIKURU
ZA BUKU LOPATULIKA**

WOPOSA CIGONJETSO

1. Aroma 8:1-8
2. Aroma 8:9-17
3. Aroma 8:18-26
4. Aroma 8:26-39
5. 2 Petro 4:4-6, Aroma 8:32
6. Aroma 10:8-13
7. Aroma 10:14-17

MTENDERE WA MULUNGU


1. Afilipi 1:2-11
2. Afilipi 1:12-18
3. Afilipi 1:18-24
4. Afilipi 2:5-11
5. Afilipi 4:1-7
6. Afilipi 4:8-14
7. Afilipi 4:15-21

NJIRA YA CIKONDI

1. 1 Akorinto 12:1-8
2. 1 Akorinto 12:9-13
3. 1 Akorinto 12:14-26
4. 1 Akorinto 12:27-31
5. 1 Akorinto 13:1-7
6. 1 Akorinto 13:8-13
7. 1 Yohane 2:7-11

KUITANA KWAKUKURU

1. Yesaya 55:1-5
2. Yesaya 55:6-11
3. Yesaya 55:12-13
4. Mateyu 11:28-30
5. Cibvumbulutso 1:5-8
6. Cibvumbulutso 22:1-7
7. Cibvumbulutso 22:12-17



**NDIME ZA ZIKURU-ZIKURU
ZA BUKU LOPATULIKA**

GREAT PASSAGES OF THE BIBLE
(CHINYANJA)

FIRST PUBLISHED
JANUARY 1981

BY THE
BAPTIST PUBLISHING HOUSE
P.O. BOX 31995
LUSAKA, ZAMBIA

TATE WA CIKONDI

1. Luka 15:1-7
2. Luka 15:8-10
3. Luka 15:11-24
4. Luka 15:25-32
5. 1 Yohane 3:1-3
6. Yohane 3:16-21
7. Aroma 10:1-13

NJIRA YA CIMWEMWE

1. Mateyu 5:1-12
2. Mateyu 5:13-20
3. Mateyu 5:21-30
4. Mateyu 5:31-42
5. Mateyu 5:43-48
6. Macitidwe 5:40-42
7. 2 Timoteo 2:11-15

MAPEMPHEREDWE

1. Mateyu 6:1-4
2. Mateyu 6:5-13
3. Mateyu 6:14-21
4. Mateyu 6:22-27
5. Mateyu 6:28-34
6. Luka 18:1-8
7. Luka 18:9-14

NJIRA, COONADI NDI MOYO

1. Yohane 14:1-7
2. Yohane 14:8-11
3. Yohane 14:12-17
4. Yohane 14:18-24
5. Yohane 14:25-31
6. Mateyu 25:31-36
7. Yohane 6:32-40

tso cace codabwitsa ciri copezeka. Tsopano ali okonzeka ndi okonzekera kukhululukira. LERO ciombolo ciri kudikhira kuti cilandiriridwe. Tsiku la MAWA lingakhale locedwa.

KUWERENGA BUKU LOPATULIKA TSIKU NDI TSIKU

PACIYAMBI MULUNGU

1. Genesis 1:1-13
2. Genesis 1:13-26
3. Genesis 1:26-2:3
4. Masalmo 100
5. Yohane 1:1-4
6. Akolose 1:15-20
7. Yeremiya 10:12-13, 27:4-5

MBUSA WABWINO

1. Masalmo 23
2. Yohane 10:1-6
3. Yohane 10:7-15
4. Yohane 10:27-30
5. Masalmo 3:1-6
6. Masalmo 27:1-6
7. Masalmo 84:1-4, 10-12

MTUMIKI WOSAUTSIDWA

1. Yesaya 53:1-6
2. Yesaya 53:6-12
3. Afilipi 2:5-11
4. Macitidwe 8:26-35
5. Macitidwe 8:35-40
6. 1 Petro 2:21-25
7. Aroma 8:31-34

NDIME ZA ZIKURU-ZIKURU ZA BUKU LOPATULIKA

PHUNZIRO

TSAMBA

1. PACIYAMBI - MULUNGU.....1
2. MBUSA WABWINO 4
3. MPULUMUTSI WOSAUTSIDWA.....8
4. TATE WACIKONDI.....12
5. NJIRA YACIMWEMWE.....16
6. MAPEMPHEREREDWE.....19
7. NJIRA, COONADI, NDI MOYO.....23
8. WOPOSA CIGONJETSO.....26
9. MTENDERE WA MULUNGU.....30
10. NJIRA YACIKONDI.....35
11. KUITANA KWAKUKURU.....40

PHUNZIRO 1

PHUNZIRO LA MIYEZI INO: NDIME ZA ZIKURU-ZIKURU
ZA BUKU LOPATULIKA

MUTU WA LERO: PACIYAMBI - MULUNGU

Ndime Yolingalira: 2 Akorinto 5:17

MAU APAMTIMA: *"Ndipo anaziona Mulungu zonse zimene
adazipanga, ndipo, taonani, zinali za
bwino ndithu."*

Genesis 1:31

Ndime Zowelenga: Genesis 1:1-2:3

MTSOGOLERI:

Kodi ndani amene analenga dziko? Anthu akhala ali kudabwa za yankho la funso limene-li. Iwo adaganiza kuti azibambo ndi azimai sakanakhoza kulipanga cifukwa dziko ndilalikuru kwambiri ndiponso lodabwitsa. Wina wace wa mphamvu koposa m'mene ife tiriri ayenera kulipanga. Popeza anthu sanali kudziwa kuti munthu wina waceyo ndi ndani, anapanga nthano za iye. Pamene dziko linali kupangidwa panalibe wina wace koma Mulungu yekha, amene anapanga. Koma tsiku lina, Mlengi wa dziko, Mulungu woona, anauzira munthu ndi mphamvu yace kuti alembe mbiri ya cilengedwe. Mbiri ya cilengedwe imeneyi idalengedwa mu buku loyamba la Buku Lopatulika, buku la Genesis.

GAWO 1: "PACIYAMBI"

Mlembi wa Genesis anauziridwa kulemba kuti, "paciyaambi Mulungu adalenga kumwamba ndi dziko lapansi" (Genesis 1:1). Ndime yoyambayo ndiyofunika kwambiri mu buku la Genesis. Imafotokoza momveka bwino kuti Mulungu woona ndiye mlengi wa zinthu zonse. Dziko silida-

55;6-9).

Gawo la kuitana kwa kukuru kwa Mulungu ndi kupereka kwa cikhululukiro. Ambuye Mulungu ali pafupi, akhoza kupezeka, koma ife tiyenera kumufuna Iye ndi kuitana pa iye tidakali ndi mwai wotero. Tsiku lopereka cikhululukiro likhoza kupita tisanafike kukupanga maganizo athu ofuna Mulungu.

Njira yofuniramo Ambuye iri yomveka bwino. Munthu oipa ayenera kusiya njira yace yoipa, munthu wosalungama asiye maganizo ace oipa, ndi "kubwerera kwa Ambuye" (Yesaya 55:7). Anthu ambiri anadzinyenga okha poganiza kuti pokhala ndi okhulupirira ndi olungama, zilibe kanthu kuti kaya akukhala moyo wotani. Koma kutembenuka kwanthunthu pa maganizo athu ndi zocita ndikutembenukira kwa Mulungu kuli kofunikira. Pamene ticita zimenezi, Mulungu adzakhala ndi cifundo pa ife ndi cikhululukiro copanda malire. Cikhululukiro cimeneci ndi ca ufulu kwa ogula, koma cidatengera zambiri kwa ogulitsayo. Sitiyenera kuiwala kuti Yesaya 55 amadza pambuyo pa Yesaya 53, ndi kuti mtanda vima pakati pa dongosolo la Mulungu.

MTSOGOLERI:

Palibe cimene dziko lingapereke comwe cingakhutiritse, ndalama, zokondweretsa, kumveka, mphamvu, kapena miyambo. Pamene titenga mbali ya zokondweretsa za moyo wa dziko lino, pamakhalabe kanthu kena mkati kamene kamanena kuti, "Ndiri ndi njala, Ndiri ndi ludzu." Bwanji osabvomereza kuitana kwa phwando la ufumu lomwe mfumu idakonza. Cifukwa tsopano phwando lakonzeka kale. Tsopano Mulungu ali pafupi. Tsopano cipulumu-

Sangathe kulandiridwa kapena kulimbiridwa. Zomwe Mulungu apereka ziri za ufulu, ndi Mulungu mwini. Iye tiyenera kungobwera kwa Iye ndi kulandira zomwe ali nazo za ife.

Zomwe Mulungu ali nazo za ife ziri zokwaniritisa. Zimakhala zambiri poperekedwa. Vinyo, mkaka, mkate, ndi kunenepa ndi mau amene anagwiritsidwa nchito monga zizindikiro za moyo wolembera ndi cuma ca Mulungu. Zimai-mira madalitso ocuruka amene aperekedwa kwa amene amabwera mu ufumu wa Mulungu.

GAWO 2: "MKATE WOSAKHUTITSA" (Yesaya 55:2-3)

Anthu amene amafuna zinthu zina zokhutitsa zosowa za miyoyo yao amaonetsedwa ngati kuti akuononga ndalama pa mkate umene sungathe kukhutitsa. Anthu ambiri amagwadira mafano ndi milungu yonama tsopano, monga anali kucitira m'masiku a Yesaya, kuyesa kupeza zokhutitsa. Ambiri amafuna funa zosangalatsa mphamvu, malo aulemu, kapena kudziwika kukhutitsa mu miyoyo yawo.

Koma tifunika kukhala ndi ludzu nthawi zonse osati tikhale okhutitsidwa, kapena kukhala anjala nthawi zonse ndikusakhala osadyetsedwa. "Mverani Ine mosamalitsa, nimudye cimene ciri cabwino, moyo wanu nukondwere ndi zonona. Cherani khutu lanu mudze kwa Ine, imvani, mzimu wanu nudzakhala ndi moyo," anadandaula Ambuye kupyolera mwa mneneri wace (Yesaya 55:2-3). Patapita zaka zina zambiri pambuyo pace Yesu anati, "Ndadza Ine kuti akhale ndi moyo, ndi kukhala nao ocuruka" (Yohane 10:10).

GAWO 3: "FUNSANI YEHOVA POPEZEKA IYE" (Yesaya

ngokhala mwa mwai kapena ngozi. Mulungu, kupyolera m'mau ace olankhulidwa, analenga dziko. Mau akuti "kulenga" amatanthauza kuti Mulungu adapanga cinthu mopanda kanthu kena. Dziko lino ndi la Mulungu cifukwa anadzipangira yekha. "Muyenera inu, Ambuye wathu, ndi Mulungu wathu, kulandira ulemmerero ndi ulemu ndi mphamvu; cifukwa mudalenga zonse, ndipo mwa cifuniro canu zinakhala, nizinalengedwa" (Cibvumbulutso 4:11).

GAWO 2: "NDIPO MULUNGU ADATI"

Kuyambira paciyambi, Mulungu anadziulula yekha monga Mulungu amene amalankhula. Iye amalankhula ndi ulamuliro ndi mphamvu. "Zakumwamba zinalengedwa ndi mau a Yehova, ndipo ndi mphweya wa mkamwa mwace khamu lao lonse" (Masalmo 33:6). "Ndi cikhulupiriro tizindikira kuti maiko ndi a m'mwamba omwe anakonzedwa ndi mau a Mulungu, kotero kuti zinthu zopenyeka sizinapangidwe zocokera mwa zooneka" (Ahebri 11:3). Mulungu anati, "Kuwale," ndipo kunawala. Cinthu coyamba cimene Mulungu anapatsa kwa cilengedwe cace cinali kuyera. Kuwala kumeneku sikunacokere ku dzuwa, mwezi, kapena nyenyezi, cifukwa zounikira zimenezi sizinanalengedwe kufikira tsiku lacinai. Kuwala kumeneku kunali kucokera mwa kuwala kwa Mulungu. Mdimba umene unali mdziko lapansi umene udaphimba dziko unawalitsidwa ndi kupezeke kwa Mulungu. Pamene Mulungu anabwera, mdimba unacoka. Kuwala kwa Mulungu kudzapambana dzuwa. "Ndipo sikudzakhalanso usiku; ndipo sasowa kuunika kwa nyali, ndi kuunika kwa dzuwa; cifukwa Ambuye Mulungu adzawaunikira; ndipo adzacita ufumu ku nthawi za nthawi" (Cibvumbulutso 22:5).

GAWO LACITATU: "CILENGEDWE CABWINO CA MULUNGU"

Mulungu asanalenge anthu ndi zilombo, anakonzeratu zinthu zonse zomwe zingafunikire ndi zolengedwazo. Iye analenga mlenga-lenga omwe ungamapereke mvula pa dziko lapansi, mpweya, ndi zinthu zina zomwe zikadafunikira ndi zinthu za moyo zomwe anazilenga, (tsiku laciwiri). Mlengi anasonkhanitsa madzi pamalo amodzi kupanga mtunda, (tsiku lacitatu). Mulungu adalenga mbeu zaziwisi ndi mitengo kupereka cakudya ku zamoyo zomwe analenga, (tsiku lacitatu). Mulungu adalenga dzuwa, mwezi, ndi nyenyezi kufuna kuonetsa kusiyana kwa pakati pa tsiku ndi usiku, (tsiku lacinai). Monga Ambuye wa nthawi, analenga nyengo, masiku, ndi zaka. Pamene zinthu zonse zinakonzedwa bwino, Mulungu adalenga zinthu zamoyo zomwe zikadakondwera ndi zonse zimene adazile-ngazo. Mulungu adalenga zilombo ndi maluwa pa dziko ndi m'nyanja adalenga nsomba zamitundu yonse ndi zinthu zina za moyo, (tsiku lacisanu).

GAWO 4: "MULUNGU APANGA MUNTHU"

Munthu anapangidwa potsiliza ndipo ndiye mfumu yazolengedwa zonse. "Mulungu ndipo adalenga munthu m'cifanizo cace, m'cifanizo ca Mulungu adalenga iye; adalenga iwo mwamuna ndi mkazi" (Genesis 1:27). Munthu ndi wapamwamba cifukwa anapangidwa m'cifaniziro ca Mulungu. Munthu popangidwa m'cifaniziro ca Mulungu kutanthauza kuti munthu akhoza kuganiza ndi kufika pa pfundo, akhoza kusankha, ali ndi malingaliro a za umunthu, ali ndi udindo, ali ndi nzeru zokhala wosadzikonda ndikuyamba cikondi ndi anzace. Koma cinthu ca tanthauzo

PHUNZIRO 11

PHUNZIRO LA MIYEZI INO: NDIME ZAZIKURU-ZIKURU ZA BUKU LOPATULIKA

MUTU WALERO: Kuitana Kwakukuru

NDIME ZOLINGALIRA: Mateyu 11:28-30

MAU APAMTIMA: *"Funani Yehova popezeka Iye, itanani Iye pamene ali pafupi."*
Yesaya 55:6

Ndime Zowerenga: Yesaya 55:1-3, 6-9

MTSOGOLERI:

Yesaya 55 akulankhula kwa Ayuda amene anali kukhala mu Babuloni kwa zaka zambiri. Iwo anatengedwa kupita ku Babulo monga zotsatira za nkondo. Tsopano iwo anakhala ogulitsa malonda ndi osintha zinthu m'dziko la ukapolo. Iwo anaiwala kuti Mulungu anawaitana kuti akhale ansembe. M'malo mofuna kucitira umboni Yehova Mulungu, anali kukondwera kukhala ndi milungu yacikunja. Iwo anali kutenga nthawi yawo monga anthu amalonda wofuna kupeza zinthu koposa kupereka zinthu. Kuli kwa anthu a m'masiku a Yesaya ndiponso kwa ife amene Mulungu ali kuitana maitanidwe a akuru.

GAWO 1: "IDZANI, PAKUTI ZINTHU ZONSE TSOPANO ZAKONZEKA" (Yesaya 55:1).

Kuitanaku ndi kwa amene ali ndi ludzu ndi njala. Ndi kwa anthu onse amene amva cosowa m'mitima yao nafunitsitsa kukhala ciyanjano ndi Mulungu. Ife ndife osowa "mu uzimu." Madalitso a Mulungu sangagulitsidwe kapena kugulidwa. Sangathe kupatsidwa ndi ndalama kapena njira ya kunyamula c'be.

Zimenezi ndi cikhulupiriro, ciyembekezo, ndi cikondi. Sizidzakhala zopanda nchito kapena zosafunika. Zidzakhala ku nthawi zonse. Cacikuru koposa ca zimenezi ndi cikondi. Sizidzakhala zopanda nchito kapena zosafunika. Zidzakhala kunthawi zonse. Cacikuru koposa ca zimenezi ndi cikondi.

MTSOGOLERI:

Kodi ndi m'njira zotani zimene timaone-tsa cikondi cathu ca kwa Kristu ndi ena? Kodi anansi athu ndi mabanja athu amaona cikondi ca Kristu cikufika kwa iwo kupyolera kwa ife. Nthawi zambiri timadandaula, kubwerera m'mbuyo, nsanje, ndi kuyambana ndi anthu ena. Cikondi ca Kristu sicimawalitsidwa kupyolera mu zokhumudwitsa za moyo. Umboni wathu wa Cikristu sukhalakanthu kopanda cikondi. Tiyeni tonse titsegule miyoyo yathu ku ciko-ndi ca Mulungu ca mwa Kristu kotero kuti cisefukire kwa anthu ena. Cifukwa Mulungu ndi cikondi.

koposa ndi cakuti munthu ali ndi gawo la uzimu lomwe iye angayanjane nalo ndi Mulungu. "Ndipo anazona Mulungu zonse zimene adazipanga, ndipo, taonani, zinali zabwino ndithu" (Genesis 1:31).

MTSOGOLERI:

Masalmo 100:3 amatiuza kuti, "Dziwani kuti Yehova ndiye Mulungu" Iyeyu anatilenga, ndipo ife ndife ace; ndife anthu ace ndi nkhusa za pabusa pace." Mulungu anatipanga ife. Iye amadziwa zabwino zomwe ziyenera ife. Tiyeni tipemphere pemphero loyamika cifukwa ca zomwe Mulungu anaticitira. Tiyeni timuuzze Mulungu m'mapemphero kuti tifuna kukhaladi ace ndikukhala nkhusa za pabusa pace.

PHUNZIRO 2

PHUNZIRO LA MIYEZI INO: NDIME ZAZIKURU-ZIKURU
ZA BUKU LOPATULIKA

MUTU WALERO: MBUSA WABWINO

Ndime Zolingalira: Yohane 10:27-30

MAU APAMTIMA: *"Yehova ndiye mbusa wanga, sindidzasowa."*

Masalmo 23:1

Ndime yowerenga: Masalmo 23

MTSOGOLERI:

Funsani aliyense kuti kodi amakonda ndime iti mu buku la Masalmo. Mwina iwo akhoza kuyankha kuti, "Masalmo 23." Mzimu Woyera amadzoza Davide Mfumu, imene nthawi zina inali

mbusa wa nkhusa, kulemba za mbusa wosatha amene ali wodzadza ndi cikondi ndi cisamaliro conse. Mbusa yemweyu, Ambuye wathu, amatisogolera ndi kutisamala. Iye akhoza kukhala mbusa wathu cifukwa anapereka moyo wace cifukwa ca nkhusa. "Ine ndine mbusa Wabwino; mbusa wabwino ataya moyo wace cifukwa ca nkhusa" (Yohane 10:11). Cikondi comwe cinali cacikuru koposa comwe cinatumiza Ambuye ku malo ochedwa bade ndi cacikuru mokwana kuti cikhoza kusamalira zosowa zathu tsopano. Ndicacikuru koposa kutiona ife njira yonse yakumwamba.

GAWO 1: "YEHOVA NDIYE MBUSA WANGA SINDIDZA-SOWA"

Davide akutiiza kuti amene adalenga dziko ndiye mbusa wace. Zosowa zonse za pa thupi kapena nzeru kapena zauzimu zimakwaniritsidwa ndi Mulungu. Mbusa amadziwa zosowa zathu ndipo ali ndi mphamvu yotipatsa. Mantha ocita pakufuna zinthu amacotsa anthu ambiri m'njira yoonadi ndikuwalowetsa mkhwala la la cimo. Mantha akusoweka kwa nchito, mantha a ngozi, mantha akukalamba ndi mantha ena onse amacoka tikadziwa kuti Ambuye ndiye mbusa wathu. Cifukwa Iye amatikonda ife, sitidzasaukira kupumula, zozizilita, cakudya, cikhululukiro, kutsitsimutsidwa, ciyanjano, kutsogoleredwa, ciombolo ku mantha, citonthozo mzisoni, cigonjetso pa adani, kutetezedwa m'nyengo zamabvuto, cimwemwe mwa Ambuye, mphamvu yotumikira, kapena kokhalako pakutha pa ulendo wa moyo wa dziko lino. Kodi pali kanthu kena m'dziko komwe amakasiya kakuti mzimu umakasowa? Ndimva mbusa yekha momwe zinthu zonsezi zingakwaniritsidwe. Lilemeke-

kudzitamandira." Cikondi sicisilira pa zomwe wina ali nazo kapena zomwe acita. Sici-tsata zamwini yekha. Siciidzikuza.

2. "Cikondi siciidukidwa kapena kudzikuzi." Siciidzitamanda kapena kudzikonda. Siciyada ndi kudzinenera zabwino monga mbalame yonyada ija pikoko (peacock).

3. "Cikondi sicilimbirira njira yace yokha." Sici-tsata mwai wabwino kapena phindu labwino, kapena mwai wofuna kuposa ena. Cikondi cipereka mtendere kwa anthu ena kuti akhale mwa ufulu.

4. "Cikondi sicikondwera ndi cinyengo." Sici-funa-funa nkhanu zamakangano. Cikondi sicipsya mtima. Siciidukidwa. Cikondi sicisunga mkwiyo.

5. "Cikondi sicikondwera ndicinyengo." Sici-kondwera pamene zinthu sizikuyenda bwino ndi anthu ena kapena pamene anthu alephera. Cikondi sicikondwera pamene mabanja asweka.

GAWO 4: "CIKONDI SICITHA" (1 Akorinto 13:8-13)

Cikondi sicitha. Palibe mapeto amene cikondi cingafikire. Sici-fika pa mapeto ogonjetsedwa. Sici-fika pa mapeto otsiliza colinga cace. Mphatso zina zodabwitsa tsiku lina zidzafika pa mapeto otsilizira pa zolinga zomwe zinapatsidwira ndipo zidzatha. Kumvetsetsa kwathu ndikocepa ngakhale tiri ndi mphatso zambiri-mbiri. Timaganizira monga momwe mwana amaganizira. Zifanana ndi kuyang'ana mukalilole kosaoneka bwino, zonse zioneke cimbuzi. Koma tsiku lina Mulungu adzatsegula kusazindikira kwathu. Tidzakura mwa Iye. Tidzaona bwino zonse. Padzakhalira zinthu zitatu zomwe zidzafika ku moyo wosatha.

1. "Cikodni cikhala cilezere." Cimamye-tsetsa ndikudikhira. Pa mabvuto, posowa mwai, mayesero, cikondi sicikakamiza zinthu, kapena kufuna kudzionetsera.

2. "Cikondi ndi cokoma mtima." Yesu anali kuyenda yenda alikucita zabwino. Iye anapereka zabwino zambiri ndi cifundo m'dziko lino koposa mabungwe onse angacitire." Tiyenera kukhala acifundo, othandiza ndi kusamala. Cifundo cimene cimakokera kwa Akristu ndi nchito osati kungonena mau, koma zocita.

3. "Cikondi cikondwera ndi coonadi." Cimakondwera ndi cigonjetso ca tsiku ndi tsiku m'moyo wa Mkristu. Cimakondwera pamene anthu asankha coonadi.

4. "Cikondi cikwirira zinthu zonse." Cikondi cikwirira citeteza, cisamalira za ena. Cikondi sicinenera zoipa za ena dzuwa lonse kwa anthu ena.

5. "Cikondi cikhulupirira zinthu zonse." Cimakhulupirira kwanthunthu Atate wa M'mwamba. Cimakhulupirira zabwino za munthu m'nzace.

6. "Cikondi ciyembekezera zinthu zonse." Sicidukidwa. Cithandiza munthu kupyola m'masiku obvuta.

7. "Cikondi cipirira zinthu zonse." Cikondi cikhalebe pa nthawi ya dzuwa kapena mvula. Sicisunthika. Cimatithandiza kuti tikhalebe pansu pa ulamuliro wa Ambuye kufikira kumapeto aulendo titafika. Cikondi Sicisiya

GAWO 3: "ZOMWE CIKONDI SICICITA" (1 Akorinto 13:4-8).

1. "Cikondi sicicita nsanje kapena

zeke dzina lace loyera!

GAWO LACIWIRI: "KUPUMULA NDI KUPATSIDWA ZOZI-ZIRITSA"

Iye monga mbusa wabwino, amatsogolera nkhusa zace ku busa la msipu wabwino ndikuzipatsa mpumulo ndi madzi ozizira. Dambo la msipu wobiliwira ndi madzi odikha amazipatsa mpumulo wa miyoyo yao. Davide adayenera kuganizira za nthawi ya moyo wace pamene anazindikira za cigonjetso cifukwa ca cimo ndi manyazi. Kwa caka canthunthu Davide anali obvutika, analibe mtendere m'maganizo ace kapena mu mtima kufikira pa tsiku limene anatembenuka nabvomereza cimo lace nalapa mwapemphero kwa mbusa wabwino amene adamukonda iye. Pamenepo mbusa wabwino anatsitsimutsa moyo wace, anabwezeranso cimwemwe ca cipulumu-tso cace, ndikumugwiritsanso nchito monga otsatira wa Ambuye.

Bwanji moyo wanu? Bwanji moyo wanga? Kodi ufunika kutsitsimutsidwa? Kodi udagonjetsedwa cifukwa ca cimo lina losabvomerezedwa? Kodi tafoketsedwa cifukwa timaona ngati nthawi zina taima tokha monga otsatira a Ambuye? Tiyei titembenukire kwa mbusa wabwino ndiku-pempha citsitsimutso comwe anatipatsa ife. Mbusa wabwino amafuna kutipatsa zimenezi tsopano ndi cisamaliro ca cikondi.

GAWO 3: "SINDIOPA COIPA"

Pomwe miyoyo yathu ipatsidwa zoziziritisa ndi kutsitsimutsidwa, mbusa wabwino amatitso-golera m'njira za cilungamo. Ngakhale kuti njira zimenezi zitipyoletsa m'mabvuto, mmakaiko, mzigwa za mthunzi, ndi malo angozi, mlembe wa masalmo akuti, "Sindidzaopa coipa;

pakuti Inu muli ndi ine." Monga mbusa akama-tsogolera nkhusa pakati pa mapiri oopysa kuti apite kumalo oyera ndi ku msipu, nkhusa zimayandikira kufupi ndi mbusa. Zimakhalazomvera ndi kutsatira malangizo ace, zimamvera mau ace, zimakhulupirira mwa mbusa wao.

Davide anadziwa kuti ngakhale kuti iye anali kuyenda pakati pa zoopysa zisoni makanga-no ndi zokhumudwitsa mbusa wace anali pafupi naye. Mbusa wace anadziwa njira. Davide anadziwa kuti ngati Ambuye anali womutsogolera, panalibe kanthu kena. Zonse zikanakhala bwino.

GAWO 4: "MTIMA WACIKONDI"

Davide anaona Ambuye monga wa cikondi ndi opereka gome lodzaza ndi cakudya cabwino ndi caulemu ca kwa alendo ace ndi kuwadzoza ndi mafuta onunkhila. Wolandira alendo sawacitira zabwino mtseri kuti adziteteteze, koma kuti amacita zokoma alendo ace pamaso pa adani ace. Ambuye monga olandira alendo adzateteza ndi kutipatsa osati zokha zimene tiri kuzifuna, koma zocuruka - monga momwe cikho cisefukira citadzaza.

GAWO 5: "MASIKU ONSE A MOYO WANGA"

"Inde ukoma ndi cifundo cidzanditsata masiku onse. Ndipo ndidzakhala m'nyumba ya Yehova." Izi ndi zomwe analemba wa Masalmo. Ambuye samatipatsa zosowa zathu zokha ndikutipatsa citso gozo, Iye amatiteteza kucokera kwa adani athu ndikutipatsa ciyanjano pa gome lace la ciyanjano. Iye amalonjezanso kuti kuli malo athu omwe tidzakhala pakutha pa ulendo uno ndipo timaitanidwa ndi mbusa wabwino kuti tidzakakhala moyo wathu onse ndi

Ngati tidapanga mndandanda wa mphatso zonse za uzimu zomwe tidafuna kukhala nazo ndi nchito yonse imene tikadafuna kutumikira Mulungu ndi kwa anthu anzathu kodi ikadaphatikiza ciani? Paulo atiuza kuti ngati cikondi sicingapezeke mu mphatso iri yonse ndi mu utumiki uli onse, zotsatira za zinthu zonse ndi cabe.

- (1) Kulankhula kwabwino kwa pa dziko lapansi kapena kumwamba wopanda cikondi, ndi phokoso cabe.
- (2) Mkati mwa dongosolo la Mulungu la za anthu ace ndi lopanda phindu ngati mulibe cikondi.
- (3) Kumvetsetsa kwambiri ndi cidziwitso copanda cikondi poziphatikiza sizipanga kanthu.
- (4) Munthu wocita zozizwitsa, mphatso yapadera ya Mzimu ndiyopanda phindu ngati ilibe cikondi.
- (5) Moyo wodzipereka umene umadyetsa anjala, obveka ausiwa, inde kufika pa nsonga yodzitentha thupi kapena kudzigulitsa kuukapolo; wopanda cikondi zonse ndi zabe.

Cikondi ndico cinthu cimodzi cofunika. Palibe cinthu comwe cingakhale cabwino ngati palibe cikondico. "Pakuti Mulungu anakonda dziko lapandi kotero kuti anapatsa Mwana, wace wobadwa yekha kuti yense okhulupirira Iye asataike, koma akhale nao moyo wosatha" (Yohane 3:16).

GAWO 2: "ZOMWE CIKONDI CICITA" (1 Akorinto 13:4-7).

Mulungu anasanduka munthu, nakhala osauka kuti ife tikhale olemera (2 Akorinto 8:9).

PHUNZIRO 10

PHUNZIRO LA MIYEZI INO: NDIME ZAZIKURU-ZIKURU
ZA BUKU LOPATULIKA

MUTU WALERO: NJIRA YACIKONDI

NDIME ZOLINGALIRA: 1 Yohane 2:7-11

MAU APAMTIMA: *"Ndipo tsopano zatsala cikhulupiriro, ciyembekezo, cikondi, zitatu izi; koma cacikuru ca izi ndico cikondi."*
1 Akorinto 13:13

Ndime Zowerenga: 1 Akorinto 13

MTSOGOLERI:

Paulo analemba ku mpingo wa ku Akorinto kuwathandiza mabvuto ena a ciyanjano cao. Mu mutu 12, Paulo ananena za mphatso za uzimu. Ziwalo zina za mpingo zomwe zinalandira mphatso za uzimu anali osilira ndi olongolora. Paulo anafuna kuti iwo amvetsetse kuti mphatso zawo, ngakhale kuti zinali zosiyana, zinali zocokera kwa Mulungu. Iye anafuna abwenzi ace kudziwa kuti mphatso iri yonse ndiyofunikira pokhapo ngati ipita ndi cikondi. Mphatso zathu nthawi zonse ziyenera kumagwiritsidwa molamulidwa ndi cikondi. Mutu 13 ukupereka njira yabwino ku mpingo yomwe iri njira ya cikondi (1 Akorinto 12:31).

GAWO 1: "NDIRIBE CIKONDI, SINDIPINDULA KANTHU"
(1 Akorinto 13:1-3).

Iye. Tidzakhala alendo okhalilatu m'nyumba ya Mulungu.

MTSOGOLERI:

Kodi mudzafuna kudziwa kuti mu mtima wanu muli nyumba yosamangidwa ndi manja, yosatha ili m'mwamba, ikukonzedwa ndi kuyembekezera kudza kwanu? Nyumba imeneyi ikhoza kukhala yanu ngati mutadziwa Mbusa wa bwino monga Mpulumutsi wanu. Mwana wa Mulungu adapereka moyo wace cifukwa ca ife pamtanda. Khulupirirani mwa Ambuye Yesu Kristu kuti akhale Mpulumutsi wanu ndi Mbusa wanu.

PHUNZIRO 3

PHUNZIRO LA MIYEZI INO: NDIME ZAZIKURU-ZIKURU
ZA BUKU LOPATULIKA

MUTU WALERO: MPULUMUTSI WOSAUTSIDWA

NDIME ZOLINGALIRA: 2 Akorinto 5:17-21

MAU APAMTIMA: *"Tonse tasocera ngati nkhusa; tonse tayenda yense m'njira ya mwini yekha; ndipo Yehova anaika pa Iye mphulupulu ya ife tonse."*

Yesaya 53:6

Ndime Yowerenga: Yesaya 53

MTSOGOLERI:

Yesaya 53 ndi "Uthenga" wa mu Cipangano Cakale. Umaonetsa kuti cilango ca macimo ndi kubvutika ndi imfa. Umatiuza kuti Yesu adalipira cilango cathu potisaukira ndi kutifera m'malo mwathu. Umatiuza kuti timayesedwa olungama pamaso pa Mulungu ngati

tilandira Yesu Kristu monga Mpulumutsi wathu. Ndipo amatisonyeza cigonjetso ca pa macimo comwe tikhoza kukhala naco kupyolera mwa cikhulupiriro ca pa mwana wa Mulungu, Yesu Kristu. Buku la Yesaya lidalembedwa zaka zambiri zapitazo Yesu Kristu asanabadwe. Mneneri anali otsimikiza za Kristu kuti ndiye-di nsembe yoyenera kotero kuti analemba Yesaya 53 ngati kuti zinaoneka kale.

GAWO 1: "MOYO WA MTUMIKI" (Yesaya 53:1-3).

Anthu a m'masiku a Yesaya anali kuganiza kuti amene angadzapulumutse anthu kucokera m'mabvuto ao akanakhala ngwazi ogonjetsa ndi kuononga adani ao ndikukhazikitsa ufumu wa-mphamvu pa dziko lapansi. Iwo sanakhoze kukhulupirira kuti Mtumiki wa anthu akadaye-nera kubadwa monga mwana mwa mkazi wosakwati-wa, amene anakula osadziwika ndi anthu. Pamene mtumiki anakula kukhala wamkuru panali-be kanthu kena kanasinthika pa za maonekedwe ace a thupi kuti kapena akanakhoza kukoka ena ndi maonekedwe ace. Iye analibe cizindikiro cina codabwitsa pa mutu pace. Iye sanali kubvala mabvalidwe a anthu olemera kapena mabvalidwe angwazi ya nkondo, kapena monga nduna za boma. Pamene Yesu anauza anthu kuti Iye anali olonjezedwa wa Mulungu, amene ufumu wace sunali wa dziko lino, iye anakanidwa, ananyozedwa, ndikukhomedwa pa-mtanda.

GAWO 2: "KUBVUTIKA KWA MTUMIKI" (Yesaya 53:4-6).

Pamene zobvuta za mtumiki zitatha, anthu anabvomereza kuti iye ananyamula macimo a ocimwa. Ngati mwasintha machulidwe a dzina

munthu amene anadalira pa Kristu mu ciri conse. Paulo anadziwa kuti wopanda Kristu, sakanakhoza kucita kanthu (Yohane 15:5). Koma mwa Kristu iye anakhoza kucita zinthu zonse kupyolera mwa amene adamupatsa mphamvuyo (Afilipi 4:13).

Nthawi zambiri mipingo yathu imapatsa anthu a mu mpingomo kuti aphunzitse kalasi ya Sande Sukulu, kutsogolera gulu la azimai, kutsogolera msonkhano wa mapemphero, kapena kutumikira mzigawo zina za moyo wa mpingo. Ena a ife ndife olakwa ponena kuti, "sindi-ngathe, sindidziwa macitidwe ace, kapena kunena kuti ndiri kucita mantha." Ngati ife tiri mwa Kristu tikhoza kucita zinthu zonse kupyolera mwa Iye amene amatipatsa mphamvuyo. Madalitso a Mulungu sioperewera. Nyumba yace yosungilamo imakhala yodzaza nthawi zonse ndipo imasefukira. Mulungu wathu ali olemera, iye ndi mwini wa zinthu zonse. Mulungu sadzatikhumudwitsa pofuna kutipatsa zosowa zimene tisowa. Mwa cigwirizano cathu ndi Kristu mwa cikhulupiriro tinalumikidwa ku madziko ndi zoperekedwa za cuma coonadi. Koma Paulo anatseka kalata yace ya kwa Afilipi ponena kuti "koma Mulungu wanga adzakwaniritsa cosowa canu ciri conse monga mwa cuma cace m'ulemerero mwa Kristu Yesu" (Afilipi 4:19). Ulemerero ndi mayamiko akhale kudzina lace!

MTSOGOLERI:

Tiyeni tikhale ndi kanthawi mwa pang'ono nthawi ya cete. Kristu ndiye amasinthitsa pakati pa kugonjetsedwa ndi cimwemwe, pakati pakusowa ndi kukhala ndi zambiri, pakati pa kubvutika ndi mtendere, pakati pakufoka ndi mphamvu, pakati pa kufuna ndi kukwaniritsidwa.

le ndi zolephela zimene zinabvomerezedwa ndi kukhululukidwa ndi Atate wathu wa Kumwamba, mtendere wathu udzacoka. Ngati maganizo oipa a cilako-lako ndi cifundo abwera m'maganizo athu, ndipo tingowasunga ndikuwaganizira, mtendere wathu sudzakhalakobe. Ngati wina wace waticimwira ife ndipo tipita kwa ena ndikulankhula za zimenezo ndi kupitiriza kuganiza zimenezo, kudzicinjiriza kwathu kudzapilikitsa mtendere wathu.

Paulo anauza anthu a ku Afilipi kuti aganizire zolemekezeka, zolungama, zoyera, zokongola, ndi zokoma mtima. Tiyenere kuganizira zinthu zomwe zingalemekeze Mulungu. Afilipi anali kuona Paulo pamene anali kugwira nchito, kutumikira, kuganizira, ndi kuphunzitsa. Iwo anadziwa kuti iye ali kulamulidwa ndi mzimu wa Kristu. Paulo anali ndi udindo wonena kwa iwo ndiponso kwa ife, "Zimenenso mudaziphunzira, ndi kuzilandira, ndi kuzimva, ndi kuzionana mwa ine, zomwezo citani; ndipo Mulungu wa mtendere adzakhala pamodzi ndi inu" (Afilipi 4:9). Paulo anali citsanzo cacikuru ca munthu amene anadziwa mtendere ndikukwaniritsidwa ngakhale kuti pali zinthu zina zokhumudwitsa za kunja kwa moyo wace cifukwa moyo wace udapumula mwa Yesu Kristu.

GAWO 4: "NDIKHOZA ZONSE MWA KRISTU" (Afilipi 4:12-13,19).

Paulo anadziwa kuti akanakhoza kukomana ndi zokhumba za moyo mu nyengo iri yonse kupyolera mwa Kristu amene anali kumupatsa mphamvu. Ngakhale kuti Paulo anali munthu ophunzira kwambiri, sanadalire pa nzeru zace zokha. Paulo sanali wopanga zodabwitsa kapena munthu wamphamvu mu mzimu. Iye anali

la Kristu ndikumanena kuti "Iye" zikhoza kutithandiza kuti timvetsetse.

4. Kristu ananyamula zowawa zanga ndi kusenja zisoni zanga.
5. Kristu analasidwa cifukwa ca zolakwa zanga, nakwapulidwa cifukwa ca mphulupulu zanga, cilango conditenge-ra ine mtendere cinamgwera Kristu, Ndipo ndi mikwingwirima ya Kristu ine ndaciritsidwa.
6. Ndasocera ngati nkhusa; ndayenda m'njira ya ine ndekha; ndipo Yehova anaika pa Kristu mphulupulu yanga.

GAWO 3: "IMFA YA MTUMIKI" (Yesaya 53:7-9).

Mtumiki anasautsidwa mwa nkhusa. Iye anabvutika mosakangana nao cifukwa analora kuti zitero. Kodi ndicifukwa ciani anakhala cete posautsidwa? Cifukwa iye anadziwa colinga ca Mulungu; Iye anadziwa kuti anali kubvutikira ena. Mtumiki anaweruzidwa mwamsanga ndi kuweruzidwa kuti aphedwe. Panalibe amene anaganizira kuti imfa yace inali ya macimo ao. Ngakhale pa imfa yace ciweruzo cosayenera cinapitilizika ndipo cidani sicinaleke, kufikira ku manda. Iye analibe cifukwa ndipo opanda cimo, okondedwa wa Atate. Yesu Kristu anati, "Palibe wina andicotsera uwu, koma ndiutaya Ine ndekha" (1 Yohane 10:18).

GAWO 4: "KUPAMBANA KWA MTUMIKI" (Yesaya 53:10-12).

"Koma kunakomera Yehova kumtundudza" (Yesaya 53:10). Mulungu sanakondwere ndi kubvutika kwa mtumiki; iye anapirira m'malo mofuna kubweretsa cifuniro cace -- kupereka

cipulumutso. Mtumiki olungama wa Mulungu amakhala nsembe ya ucimo ya anthu onse. Imfa yace ya nkhanza inali dongosolo la Mulungu la cipulumutso. Imapereka cipulumutso kwa anthu onse. Mtumiki osatha, amene anasautsi-dwa, anakanidwa, anaphedwa, anaukanso kwa akufa, ndipo tsopano ali ndi moyo ndipo amapempherera ocimwa. Yesu anagonjetsa Sata-na, cimo, ndi imfa. Iye amapatsa cigonjetso kwa onse amene amakhulupirira mwa Iye.

MTSOGOLERI:

"Mukhale nao mtima mkati mwanu umene unalinso mwa Kristu Yesu, ameneyo, pokhala nao maonekedwe a Mulungu, sanaciyesa colanda kukhala wofanana ndi Mulungu, koma anadzikhuthula yekha, natenga maonekedwe a kapolo, nakhala m'mafanizidwe a anthu; ndipo popezedwa m'maonekedwe ngati munthu, anadzicepetsa yekha, nakhala womvera kufikira imfa, ndiyo imfa ya pamtanda" (Afilipi 2:5-8).

ZOCITACITA:

Gawanani m'magulu awiri. Gulu lina liwerenga ulosi kapena (zomwe Yesaya ananena kuti zidzacitika) ndi gulu lina liwerenge ndime za mu Cipangano Catsopano.

Yesaya 53:12	Luka 22:37
Yesaya 53:7	Macitidwe 8:32
Yesaya 53:8	Macitidwe 8:33
Yesaya 53:5	Aroma 4:25
Yesaya 53:1	Aroma 10:16
Yesaya 52:15	Aroma 15:21
Yesaya 53:9	1 Petro 2:22
Yesaya 53:7	1 Petro 2:23
Yesaya 53:5	1 Petro 2:24
Yesaya 53:6	1 Petro 2:25

ndi malo amizinda ndi midzi ina kukalalikira uthenga wa Kristu. Ndipo tsopano, masomphe-nya anali kumuonekera mkati mwa ndende, anamuonetsa dziko lonse monga la Kristu, "kondwerani mwa Ambuye, nthawi zonse, ndi-bwerezanso, kondwerani."

GAWO 2: "MTENDERE WA MULUNGU" (Afilipi 4:6-7).

Paulo atiphunzitsa kuti yankho la mabvuto athu ndi madandaulo ndi kukhulupirira mapemphero. Tenganani mantha anu onse, mabvuto anu, madandaulo anu onse ndikupatsa Ambuye m'mapemphero, "ndi ciyamiko." Pemphe-rani mothokoza, Paulo akuti osati mwakuda nkhwawa, osati mokakamiza. Musade nkhwawa kuti zitenga nthawi yaitali kotani kuti Mulungu acite comwe mukumupempha kuti acite. Koma, mwai wopita ku mpando wa Mulungu mwa mapemphero, khalani othokoza.

"Ndipo mtendere wa Mulungu wakupambana cidziwitso conse, udzasunga mitima yanu ndi maganizo anu mwa Kristu Yesu." Kukhala m'moyo wokhulupirira mapemphero udzadzaza mitima yathu ndi maganizo athu ndi mtendere wa Mulungu. Mtundu wa mtendere wa Mulungu uposa cidziwitso cathu. Uli monga msilikali amene adikhira pa cipata ca moyo wathu, kutsimikiza kuti palibe cina cingalowe comwe cingasokoneze ciyembekezere cathu ndi mpumulo, mtendere wathu wa mtima ndi malingaliro a mwa Yesu Kristu.

GAWO 3: "LINGALIRANI PA ZINTHU IZI" (Afilipi 4:8-9).

Maganizo athu akhoza kutilanda mtendere wa mtima ndi malingaliro amene Yesu amapereka. Ngati tipitiliza kuganiza zolakwa zaka-

zambiri. Pamene Pauli anali ku Yerusalemu kusunghetsa ndalama za Akristu osauka anazungululidwa ndi anthu ndipo akanaphedwa ngati mkuru wa ci Roma akadapanda kuwaletsa anthuwo ndikutumiza Paulo ku ukaidi. Pamene iye anali kupititsidwa ku ndende ya ku Roma kuckera ku Yerusalemu, chombo cimene adakweramo cinaonongeka ndi namondwe. Pa nthawi imene anali kulemba Afilipi, Paulo anali atadikhira kwa zaka ziwiri kuti aweruzidwe. Iye anamangidwa unyolo kwa msilikali wa ci Roma. Komabe kalata yace inadzaza ndi mau a cikondi ndi cimwemwe.

GAWO 1: "KONDWERANI MWA AMBUYE NTHAWI ZONSE" (Afilipi 4:4-8).

Kodi Paulo anali ndi ciani comwe cidamunenetsa kuti "Kondwerani mwa Ambuye?" Iye anali munthu osauka. Iye anasiya zonse cifukwa cotsatira Yesu -- cuma cace, nchito yace monga mkuru wa ansembe, mwai wace monga mfulu wa dziko ndi zabwino za pa nyumba. Iye adawerengera zonse monga zopanda pace powengerera cuma cakudziwa Yesu Kristu (Afilipi 3:7-9). Iye anadwala pafupi fupi ndi imfa. Iye anali m'ngozi ya chombo comwe cinasweka. Ndipo tsopano iye anali mkaidi womangidwa mu cingwe (cheni) ndi msilikali wa Aroma. Koma tipeza Paulo akukondwera ndikupereka ciyamiko kuti pokhala m'ndende kwamupatsa mpata wofalitsira uthenga, kuti anafikira kweni kweni asilikali amitundu, ndikuti Akristu ena analimbikitsidwa kuti akhale olimba mtima polankhula mau a Mulungu.

Kodi cinsinsi ca cimwemwe ndi mtendere wa Paulo ndi ciani? Paulo anali munthu wa masomphenya. Masomphenya amenewa anamupititsa ku Akorinto, Aefeso, Akolose, Afilipi,

Yesaya 53:4
Yesaya 53:1

Mateyu 8:17
Yohane 12:38

PHUNZIRO 4

PHUNZIRO LA MIYEZI INO: NDIME ZAZIKURU-ZIKURU ZA BUKU LOPATULIKA

MUTU WALERO: TATE WACIKONDI

NDIME YOLINGALIRA: 1 Yohane 3:1

MAU APAMTIMA: *"Ndidzanyamuka ndipite kwa atate wanga, ndipo ndidzanena naye, Atate, ndinacimwira kumwamba ndi pamaso panu."*

Luka 15:18

Ndime Zowerenga: Luka 15:11-32

MTSOGOLERI:

Nthawi zambiri Yesu anali kugwiritsa fanizo pofuna kufotokoza za coonadi cakumwamba. Nkhani ya mwana olowerera" ndi nkhanu ya cikondi ca Mulungu. Mulungu sadzakwaniritsidwa kufikira zinthu zonse zitacitika kuti kucenjeza otaika, kufuna otaika, kapena otaika ndikuwabweretsa kwa Iye kupyolera mwa Yesu Kristu.

GAWO 1: MUDZI OKONGOLA

Atate anali ndi ana awiri a amuna. Anali kukhala m'nyumba yokongola ndipo munali zakudya zambiri. Mwana wamwamuna wa m'ng'ono anatopa kukhala panyumbapo ndipo anafuna kukhala waufulu kucoka muulamuliro wa atate ace. Iye anafunsa atate ace kuti amupatse gawo la cuma cace kuti acoke kupita kumalo ena

kutali. Ndalamazo zinayenera kugawidwa pakati pa ana awiriwo atate ao atafa. Atatewo anali kufuna kuti mwana wace akhale pafupi. Iye anali osakondwa podziwa mabvuto amene akanabwera pa mwana wam'ng'ono. Koma Atate sanakakamize cifuniro cace pa mwana wace. Iye anamupatsa gawo lace loyenera kupatsa kwa mwana wačiwiri.

GAWO 2: DZIKO LAKUTALI

Mwana wa m'ng'onoyo anapita ku dziko lakutali kucokera kwa atate ace. Tsopano anakhoza kukhala monga anafunira. Kudziko lakutali panalibe wina akanamuuza kuti zomwe anali kucitazo zinali zoipa. Iye analibe mwai okhala ndi ndalama zambiri kapena abwenzi ambiri. Posacedwa ndalama zace zonse zinatha ndipo abwenzi ace onse anamusiya. Munali njala m'dzikomo. Posacedwa mwanayo anayamba kumva njala kotero kuti anapita nayamba nchito yodyetsa nkumba. Ayuda anali kukhulupirira kuti nkumba ndi nyama zodetsedwa ndipo analibe kanthu kocita ndi nkumba. Komabe mwanayo anali ndi njala ndipo anali kufuna kudya cakudya comwe anali kudyetsa nkumba.

GAWO 3: KULAPA KWA MWANA

Pamene mwana wa m'ng'ono anayamba kudya cakudya ca nkumba anayamba kuganizira ubwino wa zinthu za kunyumba kwace. Iye anali ndi atate amene anali kumukonda. Kunali zakudya zambiri ndi anchito othandiza. Iye anazindikira kuti kunali kwabwino kukakhala wanchito wa atate ace koposa kufa ndi njala m'khola la nkumba. Iye anaona m'mene anacimwira atate ace ndi kumwamba. Iye anaganizira zobwerera kupitanso kwa atate ace ndikukapempha cikulu-

MTSOGOLERI:

Cikondi ca Mulungu ndi cosatha. Ndi cokhazikika ndi cosasunthika. Ndi cokwanira ndi copambana. Mulungu amatikonda ife kupyolera mwa Kristu palibe kanthu ndi zomwe zingaoneke kwa ife. Cikondi cace cimagwira nchito mu zinthu zonse zimene zimationekera ndikuti zonse zimene zimationekera zimagwira nchito ya za ubwino wathu ndi kukwaniritsa dongosolo lace. Ife ndife opambana kupyolera mwa Kristu amene adatikonda ife.

PHUNZIRO 9

PHUNZIRO LA MIYEZI INO: NDIME ZAZIKURU-ZIKURU
ZA BUKU LOPATULIKA

MUTU WALERO: MTENDERE WA MULUNGU

NDIME ZOLINGALIRA: Yohane 14:27-29

MAU APAMTIMA: *"Koma Mulungu wanga adzakwaniritsa
cosowa cuma cace m'ulemerero mwa
Kristu Yesu."*

Afilipi 4:19

Ndime Zowerenga: Afilipi 4:4-9;12,13,19-20

MTSOGOLERI:

Paulo anali mkaidi mu boma la Aroma pamene analemba buku la Afilipi. Linalembedwera mpingo umene anaukonda kwambiri ku Afilipi. Paulo anabvutika koposa cifukwa anali kulalikira uthenga wa Yesu Kristu. Anazunzidwa ndi gulu, anamenyedwa, ndikuponyedwa miyala, ndikuponyedwa m'ndende nthawi

Yesu ali m'malo aulemu kwambiri pafupi ndi Mulungu kutidandaulira m'mwamba.

GAWO 4: "PALIBE CIMENE CINGATISIYANITSE KUCOKERA KUCIKONDI CA KRISTU" (Aroma 8:35-39).

Paulo ali kufunsa funso, "Adzatisiyanitsa ndani ndi cikondi ca Kristu?" (Aroma 8:35). Iye anayamba kuchula mayesero ankhanza, zambiri zomwe iye anapyolamo, Msautso, kupsinjika, kulonedwa, njala, usiwa, zoopsya, ndi lupanga. Zimenezi sizikhoza kutisiyanitsa ndi cikondi ca Kristu. Zikhoza kutisiyanitsa kucokera ku cuma ndi moyo, kucoka ku mabanja ndi abwenzi, kucokera kucitonthozo ndi kukhala bwino. Koma sizikhudza cikondi cosasinthika ca Kristu.

Polembanso mau a Masalmo 44:22, Paulo amati mayesero amenewa ali ngati mazunzo obwera pang'ono-pang'ono. Cikuoneka ngati tiri kuphedwa dzuwa lonse, timayesedwa nkhoa zokaphedwa. Koma kubvutika kotero sikutanthauza kuti cikondi ca Mulungu casinthika kapena kuti kanthu kena katisiyanitsa kucokera ku cikondico. Timapitiliza kukhalabe mu cikondi cace, ndife ogonjetsa.

Ngakhale moyo kapena imfa izi sizingathe kutisiyanitsa ife ndi cikondi ca Kristu. M'moyo timakhala ndi Kristu; mu imfa timafa pamodzi naye; ndipo popeza timafa mwa iye, tidzaukanso pamodzi ndi Iye. Imfa ndi kwelero lotitsogolera pamaso pa Kristu. Palibe colengedwa ciri conse ca Mulungu, palibe colengedwa cina, palibe mphamvu ina iri yonse, imene ingakhoze kutisiyanitsa ife ku cikondi ca Mulungu ca mwa Kristu Yesu Ambuye wathu.

lukiro. Iye anakonzekera kukapempha kuti akakhale wa nchito wogwira nchitoyo tsiku ndi tsiku.

GAWO 4: TATE WACIKONDI

Pamene mwana wa mng'onoyo anali kubwerera kunyumba, anali kuganizira zinthu zomwe akanafotokozera atate ace. Mtima wace unadzaza ndi manyazi. Iye sanayenera kuchulidwa kuti ndi mwananso. Iye anakonzekera kukauza atate ace kuti amutenge kukhala wa nchito wace. Pamene mnyamatayo anali kucoka kunyumbako anali kunena kuti, "ndipatseni." Tsopano anali kunena kuti "ndipangeni." Koma mwanayo analibe mwai wopempha kuti apangidwe kukhala wa nchito. Tate wacikondi anali kumudikhirira nthawi yonse. Atate anathamanga ndikukamulandira ndi manja awiri. Analamulira kuti amumveke minjiro ndi nsapato ndipo phwando linakonzedwa. Iye anamubveka mphete ya pabanja ku dzanja la mwanayo, "cifukwa mwana wanga uyu anali wakufa, ndipo akhalanso wamoyo; anali wotayika, ndipo wapezeka" (Luka 15:24). Mtima wa atate unadzaza ndi cimwemwe. Mulungu ali wotero. Iye amakhululukira nabweretsanso ciyanjano kwa aliyense amene abwerera kwa iye.

GAWO 5: MWANA WAMKURU

Mwana wamkuru anabwera kucokera kumunda wa atate ace. Iye anamva nyimbo naona makonzedwe aphwando la mlendo wa ulemu. Ndipo anamva kuti mbale wace anabwerera ndikuti phwandolo linakonzedwera mng'ono wace. Atate anali osangalala! Mwana wa mng'onoyo anali osangalala! Nyumba yonseyo inali yokondwa. Kaduka, nsanje, ndi kudzikonda kunadzaza mu mtima mwa

mwana wamkuruyo ndipo iye sanafune kukalowa kunyumbako. Tate wacikondi anaturuka ndiku-kapempha mwana wamkuru kuti alowemo ndikukakhalana nao paphwando. Mwana wa mkuru anakana. Iye sanakondwere kuti mbale wace wabwerera kunyumba. Mwana wa mkuru anadandaula kuti panalibe kanthu ndikamodzi komwe kanacitika kwa iye ndikuti anasunga malamulo a atate ace. Atate anakumbutsa mwana wamkuruyo kuti cuma conse ndicace. Iye anakumbutsa mwana wamkuruyo za ciyanjano cao ca pa banja posintha kuti "mwana wanu uyu" kukhala kuti "mng'ono wako uyu" (Luka 15:30,32). Nkhani inatha mwana wamkuru ali kunja kwa nyumba cifukwa anakana kugawana cikondi ca atate.

MTSOGOLERI:

Mulungu ali ofanana ndi Tate wacikondi mnkhaniyi. Mulungu afunitsitsa kukhululukira ndikutsitsimutsa. Angelo m'mwamba amakondwera ngati ocimwa mmodzi apulumutsidwa. Mulungu amakonda amene ali osamvera monga mwana wa mng'ono. Iye amakondanso anthu odzilungamitsa okha ndi opanda cikondi monga mwana wamkuru uja.

Tiyeni tidzifunse tokha funso ili: Kodi timakhala okondwadi pamene tiona anthu "otai-ka" ali kubweretsedwa mbanja la Mulungu? Cikondi ca Mulungu ndi ca kwa anthu onse. Tiyeni tipemphe Mulungu kuti atitsogolere kwa otaika ndi kutithandiza kuti ticite mbali yathu yowaonetsa njira ya kumudzi.

"Ngati Mulungu ali ndi ife, adzatikaniza ndani?" (Aroma 8:31). Popeza Mulungu ali ndi ife, kulibe cifukwa cakuti ndi ndani amene angadane nafe. Kulibe mphamvu ina kuli konse yomwe iri yaikuru monga mphamvu ya Mulungu. Dziko, zathupi, ndi mdielekezi akhoza kutsutsana nafe, koma iwo sangathe kutipambana pamene Mulungu ali kumbali yathu.

Mulungu ananena momveka bwino coonadi cakuti Iye amatikonda ndi kuti ali ndi ife. Iye sanatimana Mwana wace koma anamupereka cifukwa ca ife tonse. Mulungu anaonetsera cikondi cace ca kwa ife motero, "adzalekera-nji kutipatsanso ife zinthu zonse kwaulere pamodzi ndi Iye?" (Aroma 8:32). Ngati Mulungu anapereka mwana wace kudzafera pa mtanda wankhanza cifukwa ca ocimwa, angalekerenji kutipatsa ife mphatso zocepa zomwe zingatithandize ife kukhala monga Kristu.

GAWO 3: "TINALUNGAMITSIDWA" (Aroma 8:33-34).

Mkristu analungamitsidwa ndi Mulungu mwa cikhulupiro cace ca mwa Yesu Kristu. Iye analandira cikhululukiro ca macimo. Mulungu, amene ali Oweruza wathu, ananena kuti sindifenso ocimwa, kodi ndi ndaninso angatitsutse ife? Ife ndife amene Mulungu anatisankha kuti tikhale ace mwini. Mulungu anatikhulukira ife ndipo anatipatsa cilungamo comwe tingaimapo ndi iye. "Monga kum'mawa kutanimpaha ndi kumadzulo, momwemo anatisiyanitsira kutali zolakwa zathu" (Masalmol03;12).

Kodi ndi ndani tsono amene angatitsutse ife? Ndi Yesu yekha amene ali ndi udindo wocita zimenezo. Ndipo iye sadzatitsutsa ife, cifukwa Iye ndiye adatifera ife ndipo adaukanso nakhala ndi moyo. Tsopano lino

kapena cinthu ciri conse cimene cingatisiyani-tse ndi cikondi ca Mulungu comwe ciri mwa Kristu.

GAWO 1: "COLINGA CA MULUNGU" (Aroma 8:28-30)

Paulo, mtumwi akuti, "Ndipo tidziwa kuti amene akonda Mulungu zinthu zonse zithandizana kuwacitira ubwino, ndiwo amene aitanidwa monga mwa kutsimikiza kwa mtima wace" (Aroma 8:28). Mulungu wacifundo ndi wacilungamo alalamulira miyoyo yonse. Iye akhoza kutembenuza matenda, kupsyinjika, mabvuto, kulondedwa, ndi cisoni matanthauzo a madalitso kwa amene apitiliza kumukondabe, kwa amene akufuna cifuniro cace kuti cicitike m'miyoyo yao. Sitingathe nthawi zonse kuona kuti zomwe zikuoneka zidzaonetsa zabwino. Tiyenera kukhulupirira Mulungu wacikondi; tiyenera kuyenda mwa cikhulupiriro. Coonadi cimeneci ciyenera kutitukula kuposa pa mwamba pa zobvuta madandaulo, mantha, ndi makaiko.

Mulungu anatisankha ife kuti tipulumutsidwe pomwe dziko lisanalengedwe (Aroma 8:29). Colinga cace ndi cakuti ife tiyenera kukulabe kuti tifanane ndi Yesu Kristu. Mkristu akamaganiza kwambiri za zomwe zamucitikira akhoza kuzindikira kuti sizinacokere kwa iye yekha -- zonsezi zicokera kwa Mulungu. Yesu Kristu anabwera m'dziko lino; Iye anakhalamo; Iye anapita ku mtanda; Iye anaukanso kwa akufa. Palibe ciri conse comwe tinacita kuti zimenezo zioneke; imeneyo inali nchito ya Mulungu. Tinamva nkhanu ya cikondi yodabwitsayi. Ife sitidapange nkhanayi; tidangoira ndira nkhanayi.

GAWO 2: "MULUNGU ALI NDI IFE" (Aroma 8:31-32)

PHUNZIRO 5

PHUNZIRO LA MIYEZI INO: NDIME ZAZIKURU-ZIKURU
ZA BUKU LOPATULIKA

MUTU WALERO: NJIRA YACIMWEMWE

NDIME YOLINGALIRA: Masalmo 1

MAU APAMTIMA: *"Odala ndi osauka mumzimu; cifukwa uli wao Ufumu wakumwamba."*

Mateyu 5:3

Ndime Zowerenga: Mateyu 5:1-12

MTSOGOLERI:

"M'ciphunzitsa ca pa Phiri" Yesu anaphunzitsa Akristu kuti akhoza kuzindikira cimwemwe coonadi. Cimwemwe cimeneci sicimadalira pa zomwe mungacite kapena pa zomwe mungapeze, koma pa zomwe muli mwa Yesu Kristu. Osauka mu mzimu, amene ali ndi cisoni, ofatsa, amene ali ndi njala ndi ludzu lacilungamo ca Mulungu, acifundo, oyera mtima, opanga ofunizitsa kubvutika cifukwa ca Kristu -- amenewa amakhala okondwa mu ufumu wa Kristu.

GAWO 1: OSAUKA MU MZIMU NDI ONSE OLIRA
(Mateyu 5:3-4).

Anthu ambiri amene anali kumva Yesu akulankhula anali osauka mu thupi. Koma Yesu anaphunzitsa kuti cimwemwe ndi ca kwa amene adziwa zosowa zao za uzimu. Iwo amadziwa kuti ndiosauka mu uzimu ndipo amadaliratu pa Mulungu kwanthunthu amene angawapatse zosowa zao zonse. Mulungu adzawapatsa ufumu wakumwamba. Cimwemwe ndi ca kwa amene ali ndi cisoni cifukwa ca macimo ao. Amenewa adzasangalatsidwa ndikupatsidwa mphamvu yogonjetsera cimo. "Inu, Mulungu, simudzapeputsa mtima wosweka ndi

wolapa" (Masalmo 51:17).

GAWO 2: OFATSA NDI AKUMVA NJALA NDI ALUDZU
LACILUNGAMO (Mateyu 5:5-6).

Ofatsa ndi amene amadzipereka okha kuula-
muliro wa Yesu, Mfumu, ndi kukonda malamulo
a ufumu wace. Cifatso ca pa anthu anzathu
cimatanthauza kudekha kuganizira za ena,
ndikuwacitira zabwino. Ofatsa samalanda dziko
lapansi limene amakhalamo.

Acimwemwe ndi amene ali ndi njala kapena
ludzu lalikuru pa cilungamo ca Mulungu. Ntha-
wi zambiri timafuna kupeza cimene tiri kucifuna
kwambiri. Ngati tiri ndi "ludzu la cilungamo,"
ngati tiri ndi ludzu la uzimu, Mulungu adzati-
patsa zosowa za mtima wathu. Tidzakhutitsidwa.

GAWO 3: WACIFUNDO NDI MTIMA OYERA (Mateyu
5:7-8).

Munthu wa mtima wa cifundo ali wacimwemwe
pamene akumbukira kuti cifundo ca Mulungu
cinaperekedwa kwa iye pa mtanda wa Kalivari.
Iye amadziwa cimwemwe cokhala okhululukidwa.
Munthu wacifundo amakhululukira ena. Msanariya
wacifundo ndi citsanzo cabwino ca munthu wa
cifundo. Ngakhale kuti a Samariya sanali
kuciritsidwa bwino ndi Ayuda, Msamariya wacifu-
ndo anaimea ulendo wace kuti asamalire mu Yuda
amene adamenyedwa ndi acifwamba.

Okondwa ndi amene mitima yao iri yangwiro
pamaso pa Mulungu. Mtima woyera umakhala ndi
moyo wangwiro. Ife sitingathe kufika pamaso
pa Mulungu oyera ngati mitima ndi miyoyo yathu
siiri yoyera. Ngati tifuna kudzaona Mulungu
maganizo athu, malankhulidwe, ndi makhalidwe
athu akhale angwiro.

tingapemphe ndi "ciri conse." Colinga cathu
popempha ciyenera kubweretsa ulemerero kwa
Mulungu. Ndicifukwa ca mmene Yesu Kristu
aliri, kuti tidzipempha m'dzina lace, ndiku-
khulupirira kuti adzacita.

MTSOGOLERI:

Ife tiri kukhala m'nthawi yobvuta
kwambiri, mitima yathu imabvutika kawiri-
kawiri. Tiyeni tidzikumbukira kuti Yesu ndi
njira, coonadi, ndi moyo. Iye ali ciri
conse. Amafuna kukhala mwa ife ndi kutipatsa
moyo wa Cikristu wa cigonjetso moyo umene
ungabweretse ulemerero kwa Atate.

PHUNZIRO 8

PHUNZIRO LA MIYEZI INO: NDIME ZAZIKURU-ZIKURU
ZA BUKU LOPATULIKA

MUTU WALERO: Woposa Cigonjetso

Ndime Zolingalira: 1 Yohane 3:1-2

MAU APAMTIMA: *"Koma m'zonsezi, ife tilakatu, mwa
Iye, amene amatikonda."
Aroma 8:37*

Ndime Zowerenga: Aroma 8:28-39

MTSOGOLERI:

Mu Aroma 8 muli zoonadi zodabwitsa zambi-
ri zomwe zingadzaze mitima yathu ndi ciyamiko.
Ndime yotsiliza ya mutu umenewu imatikumbutsa
kuti Mulungu ndiye akulamulira dziko lino,
kugwira nchito kutipanga ife kuti tikhale
ofanana ndi Kristu. Palibe wina aliyense

kudziwa coonadi (Masalmo 119:30). Iwo anafuna moyo wabwino. Yesu ndi njira ya kwa Atate. Yesu ndi njira ya kunyumba ya Atate ace. Yesu ndi coonadi ca za Mulungu amene amakhazika anthu mwaufulu (Yohane 8:32). Yesu ndi moyo wa Atate (Yohane 6:32-35).

Filipo anafunsa Yesu kuti awaonetse Atate. Yesu anayankha kuti, "Iye amene wandiona Ine waona Atate" (Yohane 14:9). Mukaona Yesu mwaonanso Mulungu. Mulungu anatsika pansi mwa umunthu mwa Yesu Kristu ndi kubwera m'dziko lino monga munthu. Iye sanacite manyazi kugwira nchito ya munthu. Iye anadziwa kuti kuyesedwa ndi ciani, kukhala ndi njala, kutopa, kukanidwa, ndi kubvutika. Mau a Mulungu omwe analankhula kwa anthu. Nchito zace zinali mphamvu za Mulungu zomwe zinabwera kupyolera mwa iye ndi kupita kwa anthu. Yesu anauza ophunzira ace kuti akhulupirire mwa iye.

GAWO 4: "CIRI CONSE MUKAPEMPHA" (Yohane 14:12-14).

Yesu anapereka malonjezo akuru awiri kwa ophunzira ace. Yesu anati tsiku lina ophunzira ace adzacita zomwe iye anacita, ndiponso mwina zazikuru kuposa zace. Kristu pokhala mwa ife citanthauza kuti tikhoza kuitana pa maziko a Mulungu amene Yesu anali nao. Cifukwa cimene sitigwiritsidwa nchito ndi Mulungu mwa mphamvu ndi njira yopambana ndi cakuti sitimakhulupirira ndi kudalira pa Kristu.

Lonjezo laciwiri ndilakuti pempho liri lonse, loperekedwa m'dzina la Yesu, lomwe lingabweretse ulemmerero kwa atate kupyolera mwa mwana, lidzayankhidwa. Malire a cimene

GAWO 4: OPANGA MTENDERE NDI ONSE OLONDEDWA CIFUKWA CA CILUNGAMO (Mateyu 5:9-10).

Opangitsa mtendere amachedwa a a Mulungu cifukwa ca zomwe ali kucita ndizofanana ndi zomwe Mulungu amacita. Mulungu wakhala ali wopanga mtendere wamkuru. Ciyambire cakuci-mwa kwa munthu woyamba, Mulungu wayesayetsa kumubwezera ku cilungamo cangwiro ca mwa iye yekha. Opanga mtendere amafunitsitsa kuti anthu akhale ndi mtendere ndi Mulungu ndi anthu enanso.

Odala ndi amene amalora kusautsidwa cifukwa ca Kristu ndi cilungamo cace. Opanda Mulungu safuna kuwala kwa Mulungu kuti kuunikire pa zinchito zao. Iwo safuna cilungamo kuti cisinthe makhalidwe ao, miyambo, cuma kapena makhalidwe a m'mabanja mwao. Yesu analonjeza ufumu wa kumwamba kwa amene angabvutike poyesetsa kuwanditsa Ufumu wace pa dziko lapansi lino.

GAWO 5: AMENE ABVUTIKA PONAMIZIDWA CIFUKWA CA UFUMU WACE (Mateyu 5:11-12)

Odala ndi amene akondwera pamene akunyozedwa ndi kulondedwa ndi kunamiziridwa cifukwa iwo alikutsatira Yesu Kristu. Ngati ife timabvutikira Kristu motere timaikidwa mu mndandanda wa aneneri akale, ophunzira amene "anakondwera kuti anayesedwa oyenera kunyozedwa cifukwa ca dzinalo" (Macitidwe 5:41), ndi Akristu oyambirira amene anakhala "osautsika monsemo, koma osapsinjika; osinkhasinkha, koma osakhala kakasi, olondoleka, koma osatayika; ogwetsedwa, koma osaonongeka" (2 Akorinto 4:8-9)

MTSOGOLERI:

Kutsatira Kristu nthawi zonse kumabweretsa mphotho. Osauka mu Mzimu amalandira Ufumu wa kumwamba. Amene amalira amalandira citonthozo. Anjala amadyetsedwa. Acifundo amalandira cifundo. Angwiro mtima amaona Mulungu. Opanga mtendere amachedwa ana a Mulungu. Amene amalondedwa amalandira mphotho m'mwamba.

Amene ali mbari ya ufumu wa Mulungu ndi okondwa pa dziko lapansi pano ndipo akuyang'ana nira cikondwerero cacikuru m'dziko likubweraro.

PHUNZIRO 6

PHUNZIRO LA MIYEZI INO: NDIME ZAZIKURU-ZIKURU
ZA BUKU LOPATULIKA

MUTU WALERO: MAPEMPHEREREDWE

NDIME ZOLINGALIRA: Luka 18:10-14

MAU APAMTIMA: *"Atate wathu wa Kumwamba, Dzina lanu liyeretsedwe."*

Mateyu 6:9

NDIME ZOWERENGA: Mateyu 6:5-13

"Pemphero la Ambuye" ndi citsanzo comwe Yesu anatipatsa kutithandiza mapemphereredwe. Yesu anaticenjeza kuti tisakhale "monga onyenga" (Mateyu 6:5). Ndikungocita kwa anthu. Iye anaphunzitsa kuti kungobwereza-bwereza mau amodzi-modzi sindiko kupemphera. Mulungu amadziwa kuti zosowa zathu ndi zotani. Siti-mapemphera kuti timudziwitse Mulungu zosowa zathu. Timapemphera kuti tikhale ndiciyanjano

yace. Ife tikhoza kukhulupirira Yesu ndi kudalira pa nzeru zace, nchito yace, mau ace, ndi kubweranso kwace. Yesu ndiye wotsimikiza kuti Mulungu ndi ofunitsitsa kutipatsa ife zinthu zonse zomwe anakonza kuti atipatse.

GAWO 2: "NDIDZABWERANSO" (Yohane 14:2-4).

Ophunzira anabvutika pamene Yesu anawauza kuti anali kucoka pakati pao (Yohane 13:31-38). Iwo anafuna kudziwa kumene Yesu anali kupita. Yesu anawauza kuti anali kucoka mdziko lapansi kupita kunyumba ya Atate ace. Iye anati, "M'nyumba ya Atate wanga alimo malo okhalamo ambiri" (Yohane 14:2). Cimeneci cimatiuza kuti kumwamba kuli malo a munthu aliyense. Yesu adauza ophunzira ace kuti iye adayenera kutsogola kuti apite kukakonza malo kuti iwo pobwera adzakafikira kunyumba yace. "Ndikapita -- ndidzabweranso." Yesu adzabweranso! Monga momwe anabwerera kudziko lapansi pa nthawi yoyamba ndi kuti angelo adayimba, kuti, "Ulemerero kwa Mulungu kumwamba-mwamba," Yesu adzabweranso. Kubwera kwace koyamba kunali mwana Mpulumutsi. Kubwera kwace kwaciwiri ndi monga oweruza mfumu za mafumu (1 Atesalonika 4:16 ndi Mateyu 25:31).

GAWO 3: "NJIRA, COONADI, NDI MOYO" (Yohane 14:4-11).

Tomasi adabvomekeza kuti sanali kudziwa kumene Yesu anali kupita ngakhale njira yace. Yesu anayankha kuti, "Ine ndine njira, coonadi, ndi moyo; palibe munthu adza kwa Atate, koma mwa Ine" (Yohane 14:6). Ayuda anadziwa kuti adayenera kuyenda "m'njira za Mulungu" (Masalmo 27:11). Iwo anafuna

PHUNZIRO 7

PHUNZIRO LA MIYEZI INO: NDIME ZAZIKURU-ZIKURU
ZA BUKU LOPATULIKA

MUTU WA PHUNZIRO LALERO: NJIRA, COONADI, NDI
MOYO

NDIME ZOLINGALIRA: Mateyu 25:31-36

MAU APAMTIMA: *"Yesu ananena naye, Ine ndine njira,
ndi coonadi, ndi moyo. Palibe
munthu adza kwa Atate, koma mwa Ine."*
Yohane 14:6

Ndime Zowerenga: Yohane 14:1-15

MTSOGOLERI:

Yesu anafuna ophunzira ace kudziwa kuti
m'masiku owerengeka anthu oipa adzayesa
kumuononga Iye, komanso Mulungu adzabwezera
ulemerero kwa iye yekha ndi moyo udzaperekedwa
kwa ena kupyolera mwa imfa ya mwana wace.
Yesu anaphunzitsa ophunzira ace kuti m'nthawi
ya masiku amasautso akutsogolo panali cinthu
cimodzi cokha coyenera kucita -- oyenera
kumirira cikhulupiriro cao ca pa Mulungu ndi
kukhulupirira mwa iye monga Mpulumutsi.

GAWO 1: "MUKHULUPIRIRE MULUNGU, KHULUPIRIRANI
INENSO" (Yohane 14:1).

Yesu anakhala akulankhula za imfa yace
kwa nthawi zambiri. Tsopano imfa yace inaya-
ndikira kuti ioneke. Iye anafuna kutsimikiza
kut ophunzira ace anali oikonzekera. Iye
sanafune kuti adzakhale ndi mitima yobvutika.
Yesu adapempha ophunzira ace kuti akhulupirire
mwa iye monga momwe anakhulupirira Mulungu,
cifukwa ndi cokhaci comwe cingabweretse
citonthozo ndi kulimbika pa nthawi ya imfa

ndi Mulungu ndi kumutsimikizira kuti timada-
lira pa Iye.

GAWO 1: "ATATE WATHU WAKUMWAMBA DZINA LANU
LIYERETSEDWE" (Mateyu 6:9)

Atate amene timapempherako ndi Mlengi,
Mulungu wa kumwamba, wosatha, amene ali "Ine
ndine." Sitimafika kwa Mulungu cifukwa
cakuti ndife oyenera kaya kuti nchito ziri
zabwino. Timadza kwa Mulungu m'mapemphero
cifukwa iye ndi Atate wathu ndipo ife ndife
ana ace.

Atate wathu amakhala kumwamba. Iye
sakhoza kulepheretsedwa ku zinthu za dziko
lino kapena pa zinthu za lero. Iye amaona
zinthu zomwe ziri zabwino kwa ife zotiyenera
ku zaka zonse za mtsogolo. Iye ndi atate
amene ali ndi mphamvu zonse ndipo ali okonze-
kera kusendeza thambo ndi dziko lapansi kuti
"amene akonda Mulungu zinthu zonse zithandi-
zane kuwacitira ubwino, ndiwo amene aitanidwa
monga mwa kutsimikiza kwa mtima wace" (Aroma
8:28).

M'masiku a Buku Lopatulika dzina la
munthu linali kuimira makhalidwe awo. Dzina
la Mulungu liri Loyera cifukwa iye ali
Oyeradi. Pamene tipemphera kuti "Dzina lanu
liyeretsedwe," timapemphera kuti Mulungu
adzaonetsa makhalidwe a ciyero cace, colinga
ca ciyero cace ndi cifuniro cace ca ciyero;
ndikuti tidzapereka mitima yathu kwa iye
kwanthunthu ndi ciyamiko.

GAWO 2: "UFUMU WANU UDZE KUFUNA KWANU KUCITI-
DWE, MONGA KUMWAMBA COMWECO PANSI
PANO" (Mateyu 6:10).

Pamene ife tiri kuchula mau awa popemphe-

ra timapempha kuti kulamulira kwa Mulungu kupangike m'mitima yathu, kunyumba kwathu, kumizinda yathu ndi kumidzi yathu, mu maboma athu, ndi mudziko lonse. Timapempha kuti Mulungu alamulire zinthu zonse!

Yesu anati, "Ndipo mundichuliranji Ine, Ambuye, Ambuye, ndi kusacita zimene ndizina?" (Luka 6:46). Cifuniro ca Mulungu cimacitidwa bwino bwino kumwamba. Kulibe cimo kapena kusamvera kuli konse komwe kumasonkoneza ulemerero ndi mtendere kumeneko. Okhulupirira mu ufumu wa Kristu ayenera kukhala m'njira ya makhalidwe yofuna kubwere-tsa ufumu wa Mulungu m'dziko lapansi. Pemphero limeneli sindilo longofuna kulonjeza kuti tidzafunika kucita cifuniro ca Mulungu, koma kuti tidzamvomerezanso mwa cimwemwe cifuniro ca Mulungu ca m'miyoyo yathu pomwe sicili cifuniro cathu. Monga Yesu tikhoza kunena kuti, "koma simonga ndifuna Ine, koma Inu" (Mateyu 26:39).

GAWO 3: KUPEMPHERERA ZOSOWA ZA PATHUPI (Mateyu 6:11-13)

"Mutipatse ife cakudya ca lero." Mkate umaimira cakudya ndi zosoweka zina pa moyo. Ciri coyenera kufunsa Mulungu kutipatsa zonse zomwe tikufuna cifukwa cimeneci cimaonetsa kudalira pa Iye. Ngati iye atumiza mvula ndikuwalitsa dzuwa, ndi kutipatsa mphamvu yogwirira nchito ndi nzeru yogwirira bwino nchito, Iye watipatsa cakudya cathu ca lero.

"Mutikhululukire mangawa athu, monga ifenso takhululukira amangawa anthu." Kukhululukira kumatanthauza kucotsa, kufafaniza, kupasula Mulungu amacita zonsezi pamene akukhululukira macimo athu. Ngongole yapereke-dwa. Siimasungidwiranso ife. Timapemphera

kuti Mulungu adzatikhululukira monga ifenso takhululukira amene aticimwira. Kukhululukira ndiko kuiwala, kucita monga palibe mau ena analankhulidwa kapena palibe kanthu kena kanacitika. Cimatanthauza kuti sitidzafuna kubwezera koma tidzafunitsitsa kuyanjana. Timakhululukira cifukwa ife ndife "okhululukidwa."

"Musatitengere ife kokatiyesa, koma mutipulumutse kwa oipayo." Tapempha Mulungu kuti atikhululukire zolephera zathu, zolakwa zathu, ndi macimo athu. Podziwa kufoka kwathu ndi dziko la ucimo lomwe timakhalamo, timapempha Mulungu kuti mphamvu zace zitithandize kuti tisadzipereke kapena kugwa m'mayesero. Timaphunzitsidwa kupempherera ciombolo kucokera kwa woipayo (Satana). Cifukwa ca Ufumu wa Mulungu, mphamvu ndi ulemerero ndi wa nthawi zonse kwa Atate wathu wa Kumwamba.

MTSOGOLERI:

Mutawerama mitu ndi mitima muipereke kwa Mulungu m'mapemphero tiyeni tidzipereke ndipo mofatsa tibwereze pemphero la Ambuye kuganizira zinthu zonse zomwe Mzimu Woyera watiphunzitsa lero.

"Atate wathu wa Kumwamba, Dzina lanu liyeretsedwe. Ufumu wanu udze kufuna kwanu kucitidwe, monga Kumwamba comweco panso pano. Mutipatse ife lero cakudya cathu calero. Ndipo mutikhululukire mangawa athu, monga ifenso takhululukira amangawa anthu. Ndipo musatitengere kokatiyesa, koma mutipulumutse kwa woipayo. Cifukwa mwa inu muli ufumu, ndi mphamvu, ndi ulemerero ndi wa nthawi zonse. Amen."